# Phunziro 8: Mphamvu ya Kuukitsidwa kwa Khristu

## A. Choonadi chofunika kwambiri cha kuukitsidwa kwa Khristu

1. 1 Akorinto 15:1-4 Kodi ndi choonadi chofunika kwambiri chiti chimene Paulo anatsindika chokhudza imfa ya Yesu chifukwa cha machimo athu? (onaninso Aroma 1:1-4)
2. Kodi Paulo anapereka umboni wotani wotsimikizira kuti Yesu anauka kwa akufa? 1 Akorinto 15:5-8
3. Ndichifukwa chiyani pali kusiyana kwina pakati pa olemba Uthenga Wabwino zokhudza kuukitsidwa kwa Yesu kwa akufa?
4. Kodi Yesu mwiniwake anapereka umboni wotani wokhudza kuukitsidwa kwake kwa akufa? Luka 24:44-46
5. Kodi Petro anapereka umboni wotani pa Tsiku la Pentekosti wokhudza kuukitsidwa kwa Yesu kwa akufa? Machitidwe 2:22-24

## B. Kufunika kwa kuukitsidwa kwa Yesu

1. 1 Akorinto 15:12-19 N'chifukwa chiyani kuukitsidwa kwa Yesu kwa akufa kuli kofunika kwa Mkhristu?
2. Kodi Petro anaulula chiyani kwa Korneliyo chokhudza kuukitsidwa kwa Yesu? Machitidwe 10:36-40
3. 1 Akorinto 15:20-23 Kodi kuukitsidwa kwa Yesu monga "chipatso choyamba" kumatanthauza chiyani, ndipo kuukitsidwa kwa anthu onse kudzachitika liti?
4. Kodi ndi kuti kumene tingapeze uthenga wina wouziridwa wokhudza kuukitsidwa kwa "akufa mwa Khristu" pa kubwera Kwake mu ulemerero? 1 Atesalonika 4:13-17
5. Kodi Yesu anamutsimikizira chiyani Marita chokhudza kuukitsidwa kwa akufa, ndipo Marita anayankha bwanji? Yohane 11:23-27

## C. Matupi athu tikadzaukitsidwa

1. 1 Akorinto 15:35-43 Kodi matupi athu tikadzaukitsidwa adzasiyana bwanji ndi matupi amene tili nawo panopa?
2. Afilipi 3:20-21 Kodi "thupi laulemerero" la Yesu linali lotani atangoukitsidwa kwa akufa? (Luka 24:36-43, Yohane 20:27, etc.)
3. Kodi mukuganiza bwanji za kukhala ndi thupi laulemerero lopanda matenda kapena zofooka zilizonse?

## D. Mphatso ya moyo wamuyaya

1. Kodi opulumutsidwa adzalandira liti mphatso ya moyo wamuyaya? 1 Akorinto 15:51-57
2. Poganizira za tsogolo lathu laulemerero, kodi Paulo anamulimbikitsa Timoteyo kuchita chiyani? 1 Timoteyo 6:11-16

## E. Midzikiro iwiri

1. Yesu anaphunzitsa kuti kudzakhala kuukitsidwa kuwiri kwa akufa. Yohane 5:28-29
2. Kodi chidzachitike ndi chiyani kwai wo amene adzaukitsidwe pa kuukitsidwa kwa otaika? Chivumbulutso 20:4-9
3. Kodi tingapewe bwanji mapeto omvetsa chisoni a anthu amene adzaukitsidwe pa kuukitsidwa kwa otaika? Yohane 3:16, 2 Petro 3:9, Aroma 10:13, etc.